

Danieli : 8:13-27

**Mutu : Kumasulira kwa masomphenya a nkhosa yamphongo
ndi tonde**

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero Ambuye atitsogolere ndi mau awo apaYesaya 40:28, amene akuti, “Kodi iwe sunadziwe? Kodi sunamve?Mulungu wachikhalire, Yehova, Mlengi wa malekezero a dziko lapansi, salefuka konse, salema; nzeru zake sizisanthulika.”

Mupologalamu yapita ija tinali kusanthula Danieli 8:1-13, m’mene timaunika za masomphenya a nkhosa ndi tonde. Ndipo lero pa Danieli 8:13-27, tikambirana kumasulira kwa masomphenya a nkhosa yamphongo ndi tonde.

Pamene timatsiriza pologalamu yapita ija, tinali kuona za chonyasa chiri m’kachisiwa Mulungu, chomwe chinadza ndi Antiokasi.Umu ndimomwe tidaona Antiokasiakuimika fano lake la Jupiter ndi kumaumiliza a Yuda kulambira fanolo.Tidaonanso kuti Antiokasianathirazipwidzazankhumba zipangizo za m’Kachisi wa Mulungu. Kutsindika mau amene Danieli adanena pa 11:31,

pamene anati, “Ndipo ankhondoadzamuimirira, nadzadetsa malo opatulika ndi linga lake; nadzachotsa nsembe yosalekezayo, nadzaimitsachonyansachopululutsacho.”Komanso tidaona Antiokasiakuchotsa nsembe zoperekedwapaguwa la Mulungu, zomwe Mulungu adalamulira kuti ziperekedwe m’mawa ndi m’mawa.Tsono tidaonanso kuti Antiokasi amachita chimenechi, chifukwa champhamvu ya Mulungu imamutsogolera popeza ndi kosatheka kuti m’dani achitire choipa mpingo wake, ngati sali ndi Mulungu. Ndiye tidatsindika kuti zonsezi zinali kuchitika chifukwa Mulungu akugwiritsa ntchito Antiokasi ngati mkwapulowa ana ake. Kunena kuti Israeli anachita molakwa pamaso pa Yehova, kotero kuti ichi, chinali chilango cha Yehova.Koma taonani tidanenanso kuti ngakhale woipa aone ngati kuti akupambana Mulungu, sayenera kusangalala chifukwa Mulungu akuwerenga nthawi, kotero kuti nthawi ikakwana woipawoadzayesa tsoka. Pachifukwa chimenechi tidanena kutindikokoma kuti woipayo adziwe maganizo a Yehova pamene abwererakwa Kristu.

13.Pamenepo ndinamva wina woyera alikunena; ndi wina woyera anati kwa iye uja wanenayo, masomphenya a nsembe

yopserezayachikhalire ndi cholakwachakupululutsa cha
kupereka malo opatulika ndi khamuloziponderezedwe,
adzakhala mpaka liti?

Tsopano masomphenya atha, ndiye Danieli akumva mau ochokera
kwa angelo a Mulungu, amene sanathe kuwadziwa mayina awo,
akufunsana kuti, kodi choipa chopululutsachidzapitilira kuchitika
kufikira liti? Kunena kuti, kodi Antiokasiadzapitilira kuononga
nsembe za m’Kachisi wa Mulungu ndi mzinda wa Mulungu kufikira
liti? Mwanjira ina funso likuti, kodi chipembedzo chonama cha
mafano chidzapitilira kufikira liti, kuchotsa chipembedzo choona?

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna muone kuti angelo
kapena woyera mtima a Mulungu amakhudzidwa ndi china
chilichonse chochitika mumpingo wa Ambuye. Kutsindika kuti
ngati mngeroangakhudzidwe ndi zinthu zimenezi, kulibwanji ndi
chipulumutso cha munthu? Awa, ndiwo mau amene ali pa 1 Petro
1:12, amene akuti, “Kwa iwo amene kudabvumbulutsidwa kuti
sanadzitumikira iwo wokha, koma inu ndi zinthu izi, zimene
zauzidwa kwa inu tsopano, mwaiwo amene anakulalikirani Uthenga

Wabwino mwa Mzimu Woyera, wotumidwa kuchokera Kumwamba; zinthu izi angelo alalakakusuzumiramo.”

Tsono pamene kukambirana kukuchitika pakati pa angelo, zikuonetsa kuti mngelo wina anali ndichidziwitso chokwanira kusiyana ndi mngelo winayo. Nkhani iyi, ikufanana ndi muja adafunsira Petro Yohane pa Yohane 13:24, pamene idati, “Pamene Simoni Petro anamkodola nanena naye, utiuze ndiye yani amene anena za iye.” Ndiye pamene tiganizira kuti mngelo wina anali ndi chidziwitso chokwanira, ndipo pamene tikuona kuti sanali mngelo wamba ayi, koma Kristu amene panthawi imeneyo, sanali kudziwika ndi dzina.Awa, ndiwo mau apa Oweruza 13:18, amene tikuona akuti, “Ndipo mthenga wa Yehova anati kwa iye, ufunsiranji dzina langa, popeza liri lodabwitsa?” Kutanthauza kuti dzina la Kristu ndilo lodabwitsa lomwe limadziwazinsinsi zonse. Tere, ndichifukwa chake mngelo winayo anali kufunsa choipa chopululutsa chidzakhala chili m’Kachisi wa Mulungu ndi pa anthu ake kufikira liti? Kutsimikiza kuti ngati inu ndi ine, tifuna kudziwa maganizo a Mulungu, tiyenera kufunsirakwa Ambuye Yesu Kristu,

amene akhala pachifuwa cha Atate nthawi yonse, popeza ndi momwe muli nzeru yonse yobisika kwa ife.

Tsono pafunso lakuti, kodi choipa ichi, chidzapitilira mpaka liti? Yankho lake likunena kuti, kwampulowa woipa sudzachoka pa wokhulupirira onse. Koma taonani Ambuye Yesu pa Luka 22:37, adanena mau olimbikitsa akuti, “Pakuti ndinena ndi inu, chimene chidalembedwa chiyenera kukwaniritsidwa mwa Ine, ndipo anawerengedwa ndi anthu opanda lamulo; pakuti izi za kwa Ine ziri nacho chimariziro.” Kutsimikiza kuti zinthu ziri zonse zoipa kaya zowawa pamoyo wanu ndi wanga ziri ndi chimariziro chake.

14.Nati kwa ine, mpaka masiku zikwi ziwiri mphambu mazana atatu usana ndi usiku; pamenepo malo opatulikaadzayesedwaolungama.

Tsono yankho panthawi yomwe zonyasa zidzakhala zikuchitika m’Kachisi ndi pa anthu a Mulungu, likuperekedwakwa Danieli popeza funsolilidafunsidwa m’malo mwa iye. Ndiye tikukhulupirira kuti yankholilidaperekedwakwa iye ndi cholinga chofunakuti alisungekuti pambuyo pake a Yuda anzake akapindulenalo. Kutanthauza kuti yankho limeneli likadaperekedwakwa mngelo

wofunsayo, likadakhala ndi iyeyo kotero kuti silikadakhala lothandiza kwa anthu onse. Kutsindika kunena kuti yankholi linali lofunika chifukwa linali chilimbikitso kwa a Yuda, omwe anali ndi chilakolako chofuna kudziwa nthawi yeniyeni pomwe ntchito yoyeretsa Kachisi ndi mzinda wawo zidzachitika. Ichi, ndicho chifukwa china chomwe kulembera yankho la mngelo kunali kofunika.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kunenetsa kuti angelo a Mulungu amakhala akuonetsetsazinthu zonse zochitika mumpingo wa Mulungu, kotero kuti m'chifukwa chake amafuna kudziwa nthawi yomwe zoopsa izi zidzatha. Koma sitikunena kuti angelo anali kukaikira za kutha kwa choipacho ayi, anali kufunsa m'malo mwa Danieli pofuna kumulimbikitsa.

Ndiye Ambuye akupereka yankho lakuti masautso awa adzatha; koma pakali pano apitilira mpaka masiku 2,300. Kutanthauza kuti ndiwo masautso opitilira, koma adzafika pakutha ndithu. Kutsindika kunena kuti Mulungu amaona ndi kudziwa zobvuta zomwe inu ndi ine, ngati ana ake tikuyendamo, nthawi yotheramabvutowa Iye akuidziwa bwino. Tere ndichifukwa chake

pa Chibvumbulutso 2:10, adanena kuti, “Usaope zimene uti udzamve kuwawa; taona, m’dierekezi adzaponya ena a inu m’nyumba yandende, kuti mukayesedwe; ndipo mudzakhala nacho chisautso masiku khumi.” Apa, Ambuye anali kunena kuti chisautso chilipo ndithu, koma ikafika nthawi yoikika, iwo adzakhala paufulu ndi mtendere. Kutanthauza kuti kuyeretsa Kachisi ndichinthu chabwino komanso chothandiza ana a Mulungu pamene kusinthikakukuchitika m’moyo mwawo. Kunena kuti pamene Mulungu wolungama alola choipa kugwa mumpingo wake, pamakhala cholinga chakuti alange ndi kukonza khalidwe la ana ake. Mulungu amalola izi, kuulemerero wa dzina lake, popeza panthawi yake Iye amayeretsa mpingo wake. Kutsindika mau akuti Kristu anafa, kuti mpingo wake uyeretsedwendi cholinga chakuti ukaperekedwekwa Iye wopanda chilema ndi wopanda banga.

15. Ndipo kunali, nditaona masomphenyawo, ine Danieli ndima funa kuwazindikira; ndipo taonani, panaimapopenyana ndi ine ngati maonekedwe a munthu.

16.Ndipo ndinamva mau a munthu pakati pa magombeaUlayi,
naitana nati Gabrieli, zindikiritsamunthuyu
masomphenyawo.

Danieli anaona masomphenya a nkhosa yamphongo ndi tonde,
koma sanathe kufotokonzeratanthauzo lake, kotero kuti anali ndi
chilakolako chofuna kudziwa tanthauzo lake. Kutanthauza kuti
iwo amene adziwadi zinthu za Mulungu zoonza, amakhala ndi
chilakolako chofuna kudziwa zambiri zoonza za Mulunguyo. Awa,
ndiwo anthu amene amafunafuna nthawi yonse ndipo
amachipezadi. Uku, ndikutsimikiza mau ya Ambuye Yesu pa
Mateyu 7:7, amene akuti, “Pemphani ndipo chidzapatsidwakwa inu,
funani ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo chidzatsegulidwa kwa
inu.”

Ndiye monga Danieli adapempha mu 2:18 kudzera m’pemphero,
panonsowapeza yankho kudzera mkupempha kwake. Tere
ndichifukwa chake mngelo Gabrieli akuuzidwa kuti amuuze Danieli
za kumasulira kwa masomphenyawo. Ndiye funso mkukhalapo
kuti, kodi ndani wina akanathakulamula mngelo Gabrieli, woposa
Ambuye wathu Yesu Kristu, kuti amuzindikiritse za kumasulira

kwake? Ndiye tikunena kuti nthawi zina Mulungu amakondweretsedwa kugwiritsa ntchito angelo ake, osati pachitetezo chokha, komapakuwatuma kuti apereke Uthenga umene Mulungu afuna kukwaniritsa.

17.Nayandikira iye poimainepo; atadza iye tsono ndinachita mantha, ndinagwa nkhope pansi; koma anati kwa ine zindikira, wobadwa ndi munthu iwe, pakuti masomphenyawo anena za nthawi ya chimariziro.

Danieli ndiye munthu wokhulupirika ndi wolimba mtima, amene wakhala akuona masomphenya a Mulungu kwanthawi yaitari, koma pano akuopa munthu wachilendo, amene wafika pafupi naye.Tere, Danieli wagwa pansi, osati kuti akupembedza mngelo ayi, koma chifukwa cha kuwala kwa maonekedwe aulemerero a munthuyukomanso chifukwa choonakufooka kwake. Ndipo taonani kuti pamene Danieli anagwa nkhope yakepansi, anakhala chikhalire pomwepo atathedwa nzeru ndi kugona pomwepo monga akunenera pa Danieli 10:9, kuti, “Ndipo ndinamva kunena kwa mau ake, ndipo pamene ndinamva kunena kwa mau ake

ndinagwidwa ndi tulotatikurupankhope panga, nkhope yanga pansi.”

Tsono pamene mngelo akuitanira Danieli kuti “mwana wa munthu,” sakutanthauza kuti amamutenga kuti ndiye mwana wa Mulungu ayi, koma amafuna kumuuza kuti atcherekhutu ku Uthenga umene anatengawo. Tere, ndichifukwa chake akumuuza kuti ansasefumbikumapazi ake ndikutiaimirirekutchelakhutu ku Uthenga wa Mulungu. Ndiye Uthenga ukunena kuti, “Pakuti masomphenyawo anena za nthawi ya chimariziro.” Kutanthauza kuti pali nthawi yomwe inakhazikitsidwam’tsogolomo pomwe masomphenyawaadzakwaniritsidwa.

Mau awa, ndiwo amene anathunzitsa mtima wa mneneri Danieli popeza anali kuonetsa nthawi yakutha kwa masautso ndi mayesero ya anthu, nthawi yomweyo chinalichiyambi cha kumasulidwa m’moyo watsopano monga mwachikonzero cha Mulungu. Iyi, ndiyo nthawi ya ulamuliro wa Mesiya. Mwanjira ina masomphenya awa, adzakwaniritsidwa pakutha kwa masiku 2,300 nthawi yakutha kwa ulamuliro wa Antiokasi, umene unapondereza chipembedzo cha Yehova. Iyi, ndi nkhani ya mfumu ya kum’mwera, imene

idzathirankhondo pa Antiokasi monga akunena motsindika pa Danieli 11:40, kuti, “Ndipo nthawi yotsiriza mfumu ya kum’mwelaidzalimbana naye ndi mfumu ya kumpoto idzamdzera ngati kabvumvulu ndi magareta ndi apakavalo ndi zombo zambiri; nadzalowam’maiko nadzasefukira ndi kupitirira.”

18.Ndipo m’mene analikulankhula ndi ine ndinagwidwa ndi tulotatikuru, nkhope yanga pansi; koma anandikhudza, nandiimiritsa pokhala inepo.

19.Ndipo anati, taona, ndidzakudziwitsa chimene chidzachitika pa chitsiriziro cha mkwiyo; pakuti pa nthawi yoikikampakutha pake.

Danieli mundime ino, ali ndi mantha ndipo akuonetsa kutha nzeru ndi masomphenyawa monga muja mantha adagwira Zakariya ataona mngelo wa Mulungu pa Luka 1:12. Ndiye taonani mngelo akumugwira ndi kumutchula kuti ‘mwana wa munthu.’ Kutanthauza kuti ngakhale Danieli anapatsidwa mwayi wolankhula ndi mngelo wa Mulungu, sayenera kudzikweza ayi, kotero kuti ayenera kukumbukira kuti ndiye mwana wa munthu. Tere, masomphenya adzakwanitsidwa pakutha kwanthawi.

20.Nkhosa yamphongowayiona ya nyanga ziwiri ndizo mafumu a
Mediya ndi Peresiya.

21.Ndi tondewamanyenje ndiye mfumu ya Helene, ndi
nyangayaikuruiri pakati pa maso ake ndiyo mfumu yoyamba.

22.Ndi kuti zinaphuka zinayi m'malo mwake mwa iyoitatyoka,
adzauka mafumu anayi ochokera mu mtunduwuwa anthu
koma osakhala nayo mphamvu ya uja.

Mngelo Gabrieli akupereka tanthauzo lakuti nkhosa yamphongo ija,
ya nyanga ziwiri, ikuimira ufumu wa Amedi ndi Peresiya. Pamene
tondewamanyenje, ndiye Alexander, mfumu ya Greek (Helene).
Ndipo nyanga zinayi zomwe zinameranyanga imodzi itatyoka ndi
kuuka kwa mafumu anayi amene poyamba, anali zigawo za
ufumu wa Alexander.

23.Ndipo potsiriza pake pa ufumu wawo, atakwaniraolakwa,
idzauka mfumuya nkhope yaukaliyakuzindikirazinsinsi.

24.Ndi mphamvu yake idzakhala yaikuru, koma si mphamvu
yake idzakhala yaikuru, koma si mphamvu yake yake ayi,
nidzaonongamodabwitsa, nidzakuzika, ndi kuchita ndi
kuononga amphamvuwo ndi anthu opatulikawo.

Nkhani iyi, ikukamba za kuuka kwa ulamuliro wa AntiokasiEpifane, amene anadza pambuyo pakuthyoka kwa ufumu unayi, wa a Greek (Helene). Iyi, ndi mfumu yomwe inadziwika ndi ulamuliro wa nkha, wochitira Mulungu mwano ndi chipembedzo chake. Iyeyu, ndiye nyangayaing'ono yomwe inaphukapanyanga zinayi zomwe zinathyoka.Tsono masomphenyawa akunena kuti mfumu Antiokasi adzauka pamene uchimo wa a Yuda, udzafika pachimake pamene Mulungu sadzalola kuti upyole pamenepo. Kutanthauza kuti Antiokasi ndiye adzakhala mkwapulo m'dzanja la Mulungu kukwapula a Yudawa. Kutsimikiza kuti mphamvu zonse zomwe analinazo kuononga malo achipembedzo ndi kuzunza anthu a Mulungu, zinali kuchokera kwa Mulunguyo. Tere apa, ndipo tiphunzire kuti munthu wamphamvu lero lino, asadzitamem'mphamvu zake, pokha-pokha azindikire kuti palibenso womposa iye.

25.Ndipo mwa kuchenjera kwake adzapindulitsa chinyengo m'dzanja mwake, nadzadzikuza m'mtima mwake; ndipo posatekeseka anthu, adzaononga ambiri;

adzaukiransokalongawa akalonga, koma adzathyoledwa
popanda dzanja.

Ndime ino ikunena kuti, pamene Antiokasiadzakwanitsa kuononga
chipembedzo cha Mulungu, ndipo pamene mtima wake
udzakwezeka naganiza kuti ndiye wamphamvu woyenera
kulamulira munthu wina aliyense nadzatsutsana ndi Kalongawa
akalonga onse, amene ali Mulungu amene.

Wokondedwa anzanga apaulendo ndifuna muone kuti pamene
uchimo ukula, umafikapoonetsera kugalukira Mulungu, amene ali
Mfumu ya mafumu. Koma osadziwa kuti kuthyoka komwe
adzathyokeko, kudzakhala kuthyoka kopanda dzanja la
munthu. Kunena kuti sadzafa ndi imfa ya nkhondo kapena
kuphedwa ndi munthu wamba, koma ndi dzanja la Mulungu
wamoyo.

26. Ndipo masomphenya a madzulo ndi mamawa adanenawo ndi
oona; koma iwe ubise masomphenyawo, popeza
adzachitikaatapita masiku ambiri.

27. Ndipo ine Danieli ndinakomoka ndi kudwala masiku ena;
pamenepo ndinauka ndi kuchita ntchito ya mfumu; ndipo

ndinadabwa nawo masomphenyawo, koma panalibe wakuwazindikiritsa.

Tsono pakumaliza pa masomphenyawo, Danieli adauzidwa kuti abise masomphenyawo kwa anthu aku Babulo, chifukwa a Peresiya amene akudza kudzalanda ufumu wawo, angapsere mitima a Yuda. Ichi, ndichifukwa chakuti kumasulidwakwa a Yudawa kudalengezedwa kale kuti kudzachitika ndi a Peresiya. Mau awa akutanthauza kuti zidziwitso /mabvumbulutso a Mulungu ziyenera kusungidwa bwino, kuti panthawi yake ziperekedwemoyenera ndi mokhulupirika.

Tiyeni titsirize ndi mau akuti Danieli wakhala wokhumudwa komanso wodzazidwa ndi mantha chifukwa cha masomphenyawo, koma wachenjezedwa kuti asaululekwa munthu wina aliyense. Ndiye ngakhale uthengawo udamulemera, Danieli sanasiye kutumikira kunyumba ya mfumu monga mwa nthawi yonse.

Tere, tikuphunzira kuti pamene inu ndi ine, tikhala m'dziko lino, tiyenera kukhala ndi chinthu china chake chochita ngakhale pamene tioneke kuti tikulemekezeka ndi udindo wa Mulungu. Kutanthauza kuti sitienera kunyoza ntchito yathu ya tsiku ndi

tsiku, kotero kuti iwo wolembedwa ntchito, ayenera kugwira ntchitoyomwatcheru ndi mokhulupirika.

Kwalerotilekeza pano. Ndipo timasanthula Danieli 8:13-27, m'mene timakambirana za kumasulira kwa masomphenya a nkhosa yamphongo ndi tonde.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!